

# Malo a msipu ndi kulima zakudya za ziweto

## Malangizo a alimi ang'ono

### Kodi malo a msipu n'ciyani?

Malo a msipu ndi thengo/malo pamene ziweto monga ng'ombe zingakhale kuti zidyelepo mwacitsanzo, malo papezeka udzu ndi zomela zina zamunsi zoyenelela kudyetselako ziweto.

### Kodi zakudya za ziweto n'ciyani?

Zakudya za ziweto/phesi ndi zakudya monga maphesi, udzu pamodzi ndi maphesi osauma kapena zomela zangala/mbewu zimalimidwa, kukoledwa ndipo nthawi zina zimasungidwa kudyetsela ziweto.

### Cifukwa ciyani msipu ndi zakudya za ziweto zimalimidwa?

- Pakasowa cakudya cabwino ca ziweto makamaka nyengo youma (May mpaka November).
- Msipu wacilengedwe wosakhala/kula bwino.
- Msipu ndi zakudya zodyetsela ziweto n'njila yapafupi yopezela zakudya zopatsa thanzi zofunika za ziweto kuyelekezela ndi cakudya cogulitsidwa m'masitolo.
- Kulima msipu n'zakudya za ziweto zingakhale gwelo ya ndalama mukagulitsa maphesi ndi mbewu ku alimi ang'ombe.
- Mitundu ina ya msipu kapena udzu/maphesi ingathandize kuika conde m'nthaka ndi kucepetsa kukokoloka kwa nthaka.
- Mitundu ina ya maphesi imakhala ndi nchito zambili ndipo ingabzalidwe monga malile a minda kapena zotchinga mphepo.

### Zinthu zoganzizila popanga malo a msipu ndi zakudya zodyetsela ziweto

- Zinthu zacilengedwe (cilengedwe ndi nyengo; kugwa kwamvula; cikhalidwe canthaka; ndi zina).
- Thanzi ya ziweto - malo ena odyetselako ziweto amakhala ndi vuto ya thanzi ya ziweto monga ng'ombe kufufuma mimba.
- Kuganzizila zacuma - kukonza malo a msipu ndi maphesi kungakhale kodula kulinga ogwila nchito ndi ndalama komanso zofuna zamlimi kuphatikizapo bajeti yosunga msipu/phesi pafamu yao yonse.
- Mtundu wa msipu/phesi - mtundu kapena kusakaniza mitundu kuti mulime msipu kapena maphesi zimadalila pa:
  - Cilengedwe - msipu kapena zakudya za ziweto ziyenela kusithidwa malinga ndi nyengo ya kumaloko.
  - Colinga colimila msipuwu kapena phesi - ndi kudyetsela twangoleka kuyamwa kapena kumalizitsa nyama; kukwanilitsa posowa posadziwika; kapena kupeleka ubwino wambili monga, kuletsa kukokoloka kwa nthaka, kukonza conde m'nthaka, ndi zina.
  - Kodi msipu/zakudya zodyetsela udzathilidwa ndi mvula kapena kuthiliidwa.

## Ndondomeko yokhazikitsila malo a msipu ndi zakudya za ziweto



**Kusankha malo:** Ganizilani zotsatilazi: (i) kukula kwa malo/thengo polima msipu/maphesi; (ii) mtundu mufuna kubzala - zakudya za mitengo ndi zitsamba sizilila malo aakulu kuposa udzu wa msipu; (iii) msipu/phesi zimalimidwa pamalo amodzi ndi mbewu m'munda; monga payokha; kapena m'malile a munda; (iv) malo mwasankha, kodi angabweletse mikangano mdela lanu, mwacitsanzo, malo odyetsela ng'ombe za anansi/neba.



**Kukonzeketsa malo:** nchito yokonzeketsa malo idzadalila mtundu wa msipu/zakudya za ziweto ndi kalimidwe mudzagwilitsila nchito. Kugaula n'ng'ombe kapena thilakita kungagwilitsidwe nchito kwa mtundu wa mbewu zobzala moulutsa/kuwaza. Ngati kubzala n'kokumba maenje, sewenzetsani mifolo. Kuti nthaka isasokonedwa kwambili sankhani kugwilitsila nchito geje ing'ono ngati n'kotheke.




**Kuthila Feteleza:** Kuthila feteleza wamankhwala ku msipu ndi zakudya za ziweto sizingagwile nchito n'kusunga ndalama kwa alimi ang'ono. Pamalo palibe conde m'nthaka, kuthila manyowa wa zowolela (manyowa, kompositi olo Bokashi) kungakhale njila ina yochipa. Osathila feteleza ku mbewu za msipu/maphesi oika conde cifukwa zimaika zokha Nitrogen m'nthaka.

4	Kukuluka mbewu (kg/ha)	mipata (pakati pa mz ele x m'mizele) (cm)		Nthawi yobzala		Kulowa kwa Dzenje mobzala (cm)
		Mbewu yokha/imodzi	Mbewu Zosiyana	Mbewu yokha/imodzi	Mbewu Zosiyana	
Nkasi/citedze	30 - 50	50 x 20 - 30	Pakati pa mzele - malinga ndi mbewu; mzele-20-30	Bzalani mvula ikugwa bwino	Bzalani mbewu zafika m'nkhongono	4 - 5
Zumba (Black sunnhemp)	25 - 50	Kumwaza; 20 - 30 ngati mwa-kumba mzele	Kukumba mumfola mzele - 20 - 30	Bzalani mvula ikugwa bwino	Bzalani mbewu zafika m'nkhongono	2 - 3
Nyemba	20 - 40	50-75 x 5	Pakati pa mzele — malinga mbewu; mzele - 5 - 10	Kothela kwa Dec olo kuyamba Jan	Bzalani mbewu zafika m'nkhongono	2 - 3
Nandolo	30 - 35	50 -100 x 30-35	Pakati pa mzele - malinga ndi mbewu; 50 - 100.	Bzalani mvula ikugwa bwino	Bzalani yoyamba mvula ikugwa bwino	2 - 3
Mnangali	11 - 30	50 - 100 x 10 - 15	150-180 x 50-100	Kuciyambi kwa Dec	Kuciyambi kwa Dec	2
Mulungwe	3 - 7	50 -100 m'mizele yokumba	-	Nov mpaka Jan	-	0.5
Dulu	1 - 2	Kumwaza; 50 pakati pa mzele	50 mpaka 75cm malinga ndi wa zanyemba mubzalamo	Nov mpaka Jan	-	0.5
Udzu wa Bracharia	4 - 6	Kumwaza; 50 pakati pa mzele	-	Nov mpaka Jan	-	1 - 2

**Kubzala** - Tsiku yobzala nthawi zambili imasankhidwa malinga n'nthawi idzakhwima. Mtundu umene umaca msanga umabzalidwa mosedwa, msipu umacedwa kukhwima umabzalidwa msanga. Komabe, cifukwa ca zosadziwika zakubwela kwa mvula n'kalokwedwe, kusintha kwa nyengo, kubzala msanga kukulimbikitsidwa pa mitundu yambili. Nthawi yobzala imasankhidwanso malinga ndi mmene mudzabzalila msipu kapena maphesi kaya ndi paokha kapena pa mbewu zina. Ngati n'mbewu zanyemba zikula msanga (nkasi kapena zumba) bzalani pakati pa mbewu zina zimakula mosedwa monga chimanga, mapila, mbewu zanyemba ziyenela kubzalidwa mosedwa kuti mbewu zina ziyambillile kumela.



**Kulima udzu:** Kubzala pamalo palibe udzu ndi njila imodzi yosamalila udzu. Kulima mwamsanga n'kofunika kucepetsa mpikisano ndi udzu. Kuti musunge msipu wabwino, ndi bwino kupitiliza kucotsa udzu wosafunika. Kwa mtundu wa msipu wobzalidwa m'mifolo, pangakhale kufunika kolima mwina kamodzi msipu usanakhwime/nace. Kubzala mosakaniza mitengo ya zodyetsela ziweto kapena zitsamba ndi mbewu zotchinga ndi njila ina yosamalila udzu.



**Kuteteza moto** - Kukhazikitsa malo polima msipu ndi zodyetsela ziweto n'chito yodula kwambili kunena za ndalama, anchito/ogwila nchito ndi nthawi. N'kofunika kukhala ndi cidikha/bafa (malo olowa pansu kumene kulibe udzu wouma kapena kuuma pang'ono) kuzungulila msipu kwa utali wokwana 4m kuteteza msipu/maphesi ku lupsa.



**Kukulola ndi kudyetsela udzu ziweto** - pali njila zosiyana-siyana mmene angadyetsele mayani ziweto: (a) dulani ndi kunyamula - apa zodyetsela zipatsidwa ku ziweto zisanaume. Maphesi amadulidwa akali ang'ono ndi kupeleka ku ziweto, osati kudyedwa zikali kuchile; (b) maphesi - amadulidwa ndi kusungidwa kuti mukagwilitsile nchito panthawi yosowa. Kusakaniza mbewu ziika conde m'nthaka (leguminous biomass), zotsala za mbewu, ndi udzu zimalimbikitsidwa kuti zionjezele mayani; (c) Mayani angapangidwe cimela, zodyetsela ziweto zodindidwa zili ndi cinyontho zingasungidwe pamalo posapita kwambili mphepo. Maphesi angapangidwe mwa kusindila ndi kuphimba m'dzenje ndi pulasitiki; (d) kudyetsela mwacindinji/conco - ziweto zingayende m'munda kukadya udzu wosadula conco.



Promotion of agroforestry supported by:



With support from



by decision of the German Bundestag

Prepared by: Daniel M. Kalala